MINISTRY OF NATURAL RESOURCES, ENERGY AND MINING

NTHAMBI YOWONA ZANYENGO NDI KUSINTHA KWA NYENGO


**NYENGO MSABATAYI**

**KUYAMBIRA PA 29 DECEMBER, 2025 MPAKA PA 4 JANUARY, 2026**

## NYENGO M'SABATA IKUBWERAYI

Tiyembekezere nyengo ya mvula kupitirira ndipo yamphamvu ikuyembekezeka mphepete mwa nyanja ya Malawi ndi madera ena amchigawo chakumpoto ndi pakati. Izi zikhala chonchi kamba ka dela lodzetsa mvula lotchedwa ITCZ lomwe likhale lili mdziko muno. Mvula ikuyembekezeka kupitirira mlingo wa 120mm ku Nkhotakota ndi Nkhatabay, umene uli mlingo opitirira mmene mvula imagwera mmaderawa munthawi ino. **Izi zikubweretsa chiopsezo cha madzi osefukila.**

**Mphepo ya Mwera ikhala ikuomba nthawi zina pa nyanja zathu mu sabatayi.**





*Ulosi wamvula musabata ikudzayi. Kuphatikiza masiku onse musabatayi.*

## NYENGO MU SABATA YANGOTHAYI

Kunali nyengo yamitambo ndi ya mvula yamabingu yomwe inagwa yamphamvu m'madera ambiri**.** Mvula yambiri yomwe tinalandira inachokera ku **Mchilawengo m'boma la Mzimba** yamlingo wa **141.0mm** pa **28 December 2025.**

**Komanso mvula yochuluka inagwa m'masiku atatu (26-28 December 2025) m'madera akumwera makamaka ku Nsanje ndi Chikwawa komwe inagwa ya mlingo oposa mvula ya mwezi onse wa December m'masiku amenewa. Mwachitsanzo, kwa Supuni m'boma la Chikwawa mvula yonse inagwa ya mlingo wa 177.0mm, ku Kasinthula inakwana 159.8mm ndipo kwa Lurwe ku Nsanje inafika 150.2mm.**




*Mapu akuonetsa kuchuluka kwa mlingo wa mvula ya masiku atatu kuphatikiza (26-28 December 2025)*

## MALANGIZO M'SABATALI

- **Tipewe kuoloka madzi omwe asefukira kapena omwe akuthamanga kwambiri**
- **Tisamale pogwiritsa ntchito nyumba kapena zimbuzi zomwe ndizosalimba ndipo zanyowa ndi mvula.**
- **Mvula yamabingu:** Tikhale m'malo otetezeka

*Kuti mudziwe zambiri funsani kwa: The Director, Department of Climate Change and Meteorological Services, Ministry of Natural Resources and Climate Change, P. O. Box 1808, Blantyre, Malawi. Tel: (265) 882 266 579; Email: metdept@metmalawi.gov.mw , Website: www.metmalawi.gov.mw*

**Malo osindikizira: Blantyre** **Yatulutsidwa Lamulungu pa 28 December, 2025**